# UNDUNA WA ZACHILENGEDWE NDI KUSINTHA KWA NYENGO

## NTHAMBI YOONA ZA NYENGO NDI KUSINTHA KWA NYENGO


## ULOSI WA KAGWEDWE KA MVULA M'BOMA LA KASUNGU, 2024-2025

## DZINJA LA 2024/2025 MWACHIDULE

Nyengo ya dzinja ya 2024/2025 ikuyembekezeka kukhudzidwa ndi La Nina wochepa mphamvu. La Nina ndi kuzizira kwa madzi mdera la pakati chakum'mawa kwa nyanja yamchere ya Pacific. Izi zikhala chomwechi mpaka kumayambiriro a chaka cha 2025.

Boma la Kasungu ikuyembekezeka kulandira mlingo wa mvula okhazikika kapena kuposerapo.


## October 2024




Mwezi wa October, kudzakhala kotentha komanso kopanda mvula m'madera ambiri

Komabe mvula ya chizimalupysa, yotsatana ndi mphepo ndi mphezi, ikuyembekezereka kudzagwa m'madera ochepa.


## November 2024




Mvula ya Chizimalupysa ikuyembekezereka m'madera ochulukirapo mu mwezi wa November, yomwe mlingo wake udzafike 50mm madera ambiri.


.

## December 2024




Mvula ikuyembekezereka yochulukirapo m'madera ambiri mwezi wa December, yomwe idzafikile mlingo wa pakati pa 150mm ndi 200mm. M'madera ambiri monga kwa TA Santhe, SC M'Nyanja, TA Wimbe, ndi kumwera cha kudzambwe kwa Kasungu National Park atha kulandira mvula ya mlingo okwana 250mm. Mvula yodzalira ikuyembekezereka mweziyu, makamaka kuyambira sabata yoyamba mpaka sabata yachitatu.


## January 2025




Mvula ya mlingo ochuluka yomwe mlingo wake ndi pakati pa 200mm ndi 250mm, ikuyembekezereka m'madera ambiri mwezi wa January

Pali chiopsezo cha Ng'amba yofikira sabata imodzi.


## February 2025




Madera ambiri ku Kasungu akuyembekezereka kulandira mvula ya mlingo okhazikika, omwe ndi wa pakati pa 100-250mm


Pali chiopsezo cha Ng'ambi yofikira sabata imodzi

## March 2025




Madera ambiri akuyembekezera kulandira mvula ya mlingo wa pakati pa 100-150mm. Komabe madera monga TA wimbe, Kapelula ndi Kasungu Boma adzalandira mvula ya mlingo wokwana 200mm. Madera ena mvula ikuyembekezereka kufika ku mapeto sabata yomaliza ya mwezi March 2025.

## April 2025





Mvula ya mlingo okhazikika kapena kuposera apo ikuyembekezeka mwezi wa April yomwe mlingo wake udzakhale pakati pa 50mm ndi 100mm.

Mvula ikuyembekezeka kufika ku mapeto mwezi wa April madera ambiri

Nyengo ya dzinja ya 2024/2025 ikuyembekezereka kukhudzidwa ndi La Nina wochepa mphamvu. Boma la Kasungu ikuyembekezera kulandira mlingo wa mvula okhazikika kapena kuposerapo. Mvula yodzalira ikuyembekezereka kugwa kuyambira sabata yoyamba mpaka sabata yachitatu ya mwezi wa December 2024. Mvula ikuyembekezeka kutha kumapeto a mwezi wa March mpaka sabata yachiwiri ya mwezi wa April. Nyengo ya dzinja ikuyemebekezeka kukhala yotalika ndi masiku a pakati pa 80 ndi 120. Pali chiopsezo cha ng'amba yofikila ma sabata awiri makamaka mwezi wa January ndi February.

Ndondomeko ya kagwedwe ka mvula ku Kasungu yaperekedwa pansipa

| KASUNGU | | | |
|---|---|---|---|
| MONTH | NORMAL RANGE | | FORECAST |
| OCT | 0 | 1 | 3 |
| NOV | 15 | 59 | 23 |
| DEC | 140 | 196 | 158 |
| JAN | 146 | 230 | 221 |
| FEB | 163 | 238 | 190 |
| MAR | 79 | 147 | 207 |
| APR | 9 | 27 | 36 |





**Ulosiwu udzasindikizidwanso mu mwezi wa December 2024**

**Mukafuna kudziwa zambiri lemberani kwa:**
The Director of Climate Change and Meteorological Services, P.O. Box 1808,Blantyre.
Tel +265 1 82 47 12 / Cell: +265 882 26 65 79 Email: metdept@metmalawi.gov.mw ; Website: www.metmalawi.gov.mw



Zasindikizidwa ndi thandizo lochokera ku:



© Poster Template by Genigraphics® 1.800.790.4001 www.genigraphics.com